



Writer: William R. Flowers **Hard Questions About God Series**
Editor: Emily Ann Rickard **Episode 2 of 7: Does God Care About**
Senior Editor: Dr. Art Criscoe **Me?**
Christ to the World Ministries **Copyright © 2016**
All rights reserved

DIRECTORIAL INFORMATION

CAST OF CHARACTERS:

Thomas: **Narrator, a disciple of Jesus** (voice of a mature man)
Philip: **Disciple of Jesus** (voice of a mature man)
Jesus: **The Son of God** (warm voice of a mature man)

KODI MULUNGU AMASAMALA ZA INE?

Malemba: Yohane 2:1-11

(Music: Theme music begins, then gradually fades to underscoring during comments by Program Host)

Program Host

Takulandirani ku nkhani yathu ya “Nkhani Yeniyeni.”

Pokhapokha ngati muli m’modzi wa ohcepa amene amakhala moyo wabwino, wozungulilidwa ndi zonse zakumtima kwanu, wokhala ndi antchito amene amakutetezani ku nyengo zonse zokhumudwitsa, munaona kuti dziko lapansi ndilodzala ndi abambo ndi amayi amene amakhala m’nyengo zosautsa, kuvutika tsiku ndi tsiku kuti akhale ndi moyo komanso kuti apeze chakudya ndi pogona za apabanja pawo. Funso limene amafunso silokuti, “Kodi ndidya usiku uno?” koma “koma ndidzadyanso?”

Kwa ambiri amene amakumana ndi mafunso amenewa kuti akhale ndi moyo, amakamba za Mulungu ndi ndondomeko zake zabwino za miyoyo yathu, uthenga umene umagwera m’makutu ogontha; nyengo zinawaphunzitsa kuti Mulungu alipo, koma mwina sakudziwa kapena kulabadila za nyengo zawo.

Funso limene amafunsa ndi: Kodi Mulungu amasamala za ine? Wokonedwa Mnzanfa, ngati unafunsapo funso limeneli, ndili nawe uthenga wabwino: Mulungu sadziwa kokha za iwe, koman amadziwa cheni cheni chimenea ukudutsamo. Khalani nafe pamene tikumvera gawo lachiwiri la sewero la mafunso ovuta okhuza Mulungu, kuchokera mu nkhani komanso zochitika za anthu a mu Mawu a Mulungu.

(Music: swells to indicate scene change; then fades to soft underscoring)

Notice that scene changes are depicted with music.

Scene 1

INSERT: (Sound effects: nighttime; a soft breeze and crickets chirping in the background)

Tomasi: (kufotokoza) Pamene ndinakumana ndi Yesu wa ku Nazareti koyamba, sindinali amene mungamutche kuti wophunzira wabwino. Ndinalibe maphunziro aliwonse a za chipembedzo, anzanga ndi abale pakati pa ophunzira, ndinalibe luso lapadera kapena Mphatso zimene zikanandithandiza kukhala wophunzira wabwino, ndipo koposaposa, ndinalibe chikhumbokhumbo chokhala wophunzira. Zoonza zake ndizakuti, ndikayang’ana m’mbuyo, chifukwa chimene chinandikoka kuti ndikhale m’modzi wa ophunzira chimandiseketsa ndikachiganizira, ndicho kuti: Anali mphunsitsi wachipembedzo, Rabi, ndipo ine sindinkakhulupilira Mulungu.

INSERT: (Sound effects: add a softly crackling campfire)

Tomasi: (kufotokoza, motsitsa) Komabe ndinalola, ndipo ndinakhala wophunzira wa Rabi Yesu. Ndipo zinapezeka kuti. . .sindinali ndekha pakati pa ophunzira ake amane anali ndi mafunso mkati mwake.

INSERT: (Sound effects: add soft, murmuring voices)

Filipo: Tomasi! Bwera pano!

INSERT: (Sound effects: footsteps approach, and then stop)

Filipo: Pano; khala pansi.

Tomasi: Zikomo, Filipino.

INSERT: (Sound effects: Thomas sits down on the ground by the fire)

Filipo: Tsopani – mufunse Yesu funso lako.

Tomasi: (Modabwa) Chiyani?

Filipo: Unali ndi funso la Yesu... wakumbukira?

Tomasi: Sindikudziwa zimene ukunena, Filipino.

Filipo: Inde ukudziwa. (kumukumbutsa) Dzulo...? Pamene tinali mu nzinda?

Tomasi: Ine...

Filipo: Yesu atamuchiritsa munthu wachikulire uja ku thamanda la Betisaida

Tomasi: (mwamanyazi) Oh. Lijali

Filipo: Pitoliza, mufunse.

Tomasi: Filipino, kunena zoon, sindikufuna...

Yesu: (mwachifatse) Filipino...ngati ali ndi funso, afunsa. Sukuyenera kumukakamiza.

Tomasi: Filipino, sindikufuna kumuvutitsa Yesu ndi...

Yesu: Ukudabwa kuti ndinamuyendetsa bwanji muntu amene wakhala opuwala ziwalo kwa zaka zambiri. Zinali zovuta kuti ukhulupilire zimene maso ako anaona, ndipo ukudabwa ngati sizinali za bodza

INSERT: (Sound effects: an owl hoots in the distance)

Tomasi: Inde...koma sindikanafunsa m'mene mwaneneramo...

Yesu: Osadandaula, mnzanga; sindimakhumudwa nazo. Zoonza zake ndizakuti, sikuti ukhala woyamba kukaikira. Ndi choncho, Filipino?

Filipo: (*kuseka*) Ah, ndinadziwa kuti muchita izi kwa ine, yesu.

Yesu: Uli ndi chimenea ukufuna kumuuzza mnzako, Filipino?

Filipo: Ndikudziwa kuti Yesu akunena zimene zinachitika miyezi ingapo yapitayo ku Galileya, m'nzinda waung'ono wa Kana.

Tomasi: Sindikudziwa za nkhani imeneyi.

Filipo: Inenso sindinamvepo zimene zinachitikazo. Tinali titangokumana kumene ndi Yesu ndipo tinalipo anthu atatu okha panthawi imeneyo. Tinali titamupeza kumene Nataniyeli, pamene, Yesu anatiuza kuti tonse tinaitanidwa ku ukwati ku Kana.

Yesu: (*Kuseka*) Iai, iai, Filipino; ndinaitanidwa ndi Ineyo.

Filipo: Chabwino, tonse tinapita ku ukwati ndi Yesu. Ndipamene mavuto anayamba.

INSERT: (Sound effects: the owl hoots again)

Tomasi: Mavuto?

Filipo: Inde – alendo analipo ambiri – vinyo ochepa.

Tomasi: ukutanthauza chiyani? Vinyo anawathera?

Filipo: Inde

Tomasi: (*kuseka*) ndiye... linali vuto lanu?

Filipo: Iai, iai, amene amatsogolera mwambowo sanaitanitse vinyo okwanira.

Tomasi: Ndiye munatani?

Filipo: Palibe chimenea tikanachita. Panalibepo vinyo wina malo oyandikira.

Tomasi: Ndiye... mutu wa nkhaniyi ndi chani?

Filipo: Yesu anathana nalo vutoli

Tomasi: (*mokaikira*) Anathana nalo? Anatani?

Filipo: Ana um... Anasintha madzi kukhala vinyo.

Tomasi: Kutero?

Filipo: Panali Mitsuko ikulu ikulu ya pafupi.

Tomasi: Yodzala ndi madzi

Filipo: Inde

INSERT: (Sound effects: the owl hoots again)

Tomasi: Sikuti ndi mwano, koma... unadziwa bwanji kuti anali madzi?

Yesu: (*Kuseka chapansipansi*) Chifukwa Filipino sanakhulupilire kuti ndinasintha madzi. Pamene ogwira ntchito amadutsa ndi Mitsuko kupitita kutsogolo, Filipino anazembera nalawa.

Tomasi: Kenako...?

Filipo: Kenako...anali madzi basi. Ndinakhumudwa nazo.

Tomasi: Koma...Sindikumvetsetsa. Anali madzi chabe? Ndiye kuthana ndi vutolo kuli pati?

Filipo: Ndi m'mene inenso ndinaganizira. Koma nditaima kuyan'ganitsitsa mwa chidwi, wotsogolera mwambo anatengako madziwo...nalawa.

(Music: swells to indicate scene change; then fades to soft underscoring)

INTERMISSION

Program Host: Zikomo chifukwa chokhala nafe. Mukumvera “Nkhani mkati mwa Nkhani.” Lero tikutsatira sewero la, Mafunso Ovuta okhuza Mulungu” kuchokera mu nkhani komanso zochitika za anthu a mu Mawu a Mulungu.

M'mbuyomu, m'seweroli, Tomasi analola kukhala wotsatira wa Yesu ataitanidwa ndi Yesu, nazipeza yekha pakati pa ophunzira atakumana kuzungulira moto pakutha pa tsiku. Koma Tomasi anali ndi chikaiko za Yesu, komanso nkhani zonse za Mulungu ndi zozizwa. Kwa Tomasi, taona kuti, sanali wotsimikizika kuti ankakhulupilira Mulungu, komanso ngati Mulunguyo

alipo, Tomasi sanakhulupilire kuti Mulungu amasamala chilichonse chokhuza iye. Mverani tsopano, pamene tikupitiliza.

(Music: underscoring fades out as sound effects return)

Scene 2

INSERT: (Sound effects: nighttime; a soft breeze and crickets chirping in the background, and a soft, crackling fire)

Tomasi: Ndiye...wotsogolera mwambo atalawa madziwo...?

Filipo: Anangoima kaye kwa kanthawi, naonetsa kudabwa pa nkhope yake. Ndinakanika kupuma nthawi imeneyi. Kenako, bamboo aja anamwetulira, nati, *“Aliyense amabweretsa vinyo wabwino koyambilira kenako wosakoma kumapeto alendo atamwa mokwanira.”* (Yohane 2:10)

Tomasi: Ndiye?

Filipo: Kenako anatembenuka kwa mkwati nati, *“koma mwasunga wabwino mpakana pano”* (Yohane 2:10). Sanali vinyo chabe Tomasi; koma vinyo wabwino kwambiri amene sanalawidwepo konse ayi.

Tomasi: (Kuima kaye) Mukudziwa?

Filipo: Chiyani?

INSERT: (Sound effects: Thomas abruptly rises to his feet)

Tomasi: Ndatopa nazo nkhani zanuzi

INSERT: (Sound effects: rapid footsteps retreating as Thomas walks away; murmuring voices among the surprised disciples)

Filipo: (*mawu kumveka ngati munthu akuchoka*) Tomasi! Chavuta ndi chiyani? Ukupita kuti?

INSERT: (Sound effects: the sounds of the camp fire and voices fade away as Thomas continues to walk briskly)

Tomasi: (*kudziyankhulira yekha*) Zopanda pake izi. Madzi kukhala vinyo...

INSERT: (Sound effects: distant running footsteps, approaching; Thomas continues to walk)

Filipo: (*kumvekera patali*) Tomasi! Tomasi, tadikira!

INSERT: (Sound effects: running footsteps grow louder)

Filipo: (*kumvekera pafupi*) Tomasi! Taima!

INSERT: (Sound effects: Thomas stops, and Philip races up)

Tomasi: Ukutanthauza chiyani?

INSERT: (Sound effects: Philip stops, out of breath)

Filipo: (kumveka kuti wathedwa mpweya) Chifukwa . . . chifukwa chiyani unachoka motero?

Tomasi: Tamvera, Filipino – sindili m’modzi wa inu. Ine ayi

Filipo: (kudikira kaye kuti Tomasi amalize) Suuli . . . Chiyani?

Tomasi: Pepa, sindikukhulupilira zimenezo

Filipo: Koma ndinaziona ndi maso angawa. Ndinalawa madziwo, ndiponso ndinalawa vinyo amene anali m’mtsuko womwewo. Chinali chozizwa.

Tomasi: Chabwino. Iweyo ukukhulupilira. Ine sindinaziona zimenezi ndiye sindikukhulupilira.

Filipo: Koma unamuona Yesu akuchiritisa wopuwala ziwalo ku Yerusalemu.

Tomasi: Ndilibe chitsimikizo pa zimene ndinaona

INSERT: (Sound effects: silence between the two for a moment; we still hear the sounds of the night)

Filipo: (cha pansi pansi) Vuto ndi chiyani Tomasi? Chikukuvuta ndi chiyani?

Tomasi: Ine...

Filipo: (Cha Pansi pansi) Ndi chiyani?

Tomasi: Kodi zimenezi ndi za ntchito yanji, Filipino?

Filipo: Ukutanthauza chiyani?

Tomasi: Ngati amapanga zozizwa, ngati Yesu amasintha madzi kukhala vinyo, zimenezi zikutsimikizira chiyani?

Filipo: Zikutitsimikizira kuti Yesu anatumizidwa ndi Mulungu, sichincho?

Tomasi: (kukweza mawu pang'ono) Zoonaa? Chabwino, ngati zili chomwecho, Mulungu anamutumiza chifukwa chiyani?

Filipo: Kudzationetsera kuti Mulungu amasamala za ife.

Tomasi: (mokweza kwambiri) Kudzationetsera kuti amasamala? Amasamala? Kusintha madzi kukhala vinyo kukuonetsera kuti amasamala za ife?

Filipo: Tsopano, Tomasi, dekha...

Tomasi: (pang'onong'ono kukuwa) Vinyo akuonetsera chiyani Filipino?

Chabwino, wina aliyense analawa vinyo! Pomaliza, izi zinawathandiza chiyani anthuwo? Tsopano yesu ndiwotchuka! Bola Iyeyo!

Filipo: (*motsitsa*) Palibe amene anadziwa za chozizwachi Tomasi.

Tomasi: (*kudabwa*) Chiyani? Ukutanthauza chiyani? Ndidzachidziwikire kuti wotsogolera mwambo ankadziwa...

Filipo: Ai

Tomasi: Nanga alendo?

Filipo: Ai. Palibe amene anadziwa.

Tomasi: Sindikumvetsetsa. (*kupumira*) Nanga mkwati?

Filipo: Mwina anadziwa kuti china chake chachitika, koma...sitinamuuze.

Tomasi: (*cha pansi pansi*) Koma...nanga Yesu anachitiranji chozizwachi, ngati samafuna kuti anthu adziwe?

Filipo: Yesu sanachite izi kuti anthu ayambe kunena za Iye. Anali ndi cholinga china

Tomasi: Mwina anachitira alendo amene anali ndi ludzu.

Filipo: Ai, ngakhale aliyense anapindula m'chozizwachi, sizinali zokhuza iwo.

Tomasi: Ndiye, anachitira ndani?

Filipo: Anachitira ife, ophunzira ake; anachitira ine, Tomasi. Yesu anachitira ine chozizwachi.

Tomasi: Chiyani? Anachita choncho chifukwa chiyani?

Filipo: Ndikufunseko funso, Tomasi: unalola kumutsatira Yesu chifukwa chiyani?

Tomasi: Sindikudziwa.

Filipo: Ndipereke maganizo anga. (*kupumira*), ndikuona ngati, iweo ngatinso ine, watopa ndi ziphunzitso ndi malonjezo opanda kanthu ochokera kwa atsogoleri athu a chipembedzo; wakhala ukufuna funa china chake choti ukhulupilire, koma mpakana lero, suunachipeze. Mpakana pano.

Tomasi: Pitaliza...

Filipo: Kumutsatira Yesu chifukwa chokuti anakuitana ndi sitepe ya chikhulupiliro.

Tomasi: Sindinanene kuti ndimakhulupilira mu

Filipo: Ah, koma Tomasi, unamutsatiratu! Sukufuna kuvomereza chabe, koma izi zikuonetsera kanthu kena kokhuza iwe: zikuonetsera kuti ukufuna zambiri.

Tomasi: Izi ndi zochititsa chidwi, komano, zonsezi zikukhuzana bwanji ndi zozizwa zakezi?

Filipo: Inenso, ndakhala ndikufunafuna, Tomasi; ndipo ndimakhuupilira Yesu, ndapeza chimenea ndakhala ndikufuna: wina amene ndingaike chikhulupiliro change pa iye.

Tomasi: Mokuti umamukhulupilira Iye. Sindikuonabe kugwirizana kwake.

Filipo: Chozizwa cha madzi kukhala vinyo, chozizwa cha wopuwala ziwalo kuyenda, zonse zinali ndi cholinga chimodzi: kutsimikiza chikhulupiliro kwa amene amakhulupilira Yesu.

Tomasi: Ndiye...vinyo amene unalawayo...ukunena kuti machiritso a wachikulieyo sizinali zofunika kwa munthuyo, koma umboni chabe?

Filipo: Iai, iai, sichoncho. Machiritso anachitikadi, ndipo wopuwalayo anapindula ndithu; koma Tomasi, Mulungu analemekezeka, osati m'zozizwa zokha, komanso m'mitima ya amene akumutsatira. Cholinga cha chozizwachi chinali kutsimikiza chikhulupiliro chathu.

Tomasi: Ukundifunsa kuti ndikhulupilire kuti Mulungu amasamala za ine... chifukwa Yesu anachiritisa munthu wachikulire.

(Music: underscoring music begins softly)

Filipo: Inde, amasamala, Tomasi; amasamala za munthu wachikulieyi amene anakhala pa thamanda kwa zaka zambiri, komanso amasamala za mkwati ndi mkwatibwi amene vinyo anawathera. Ndipo Tomasi, Mulungu amasamala za iwo, mpakana anatumiza Yesu kwa iwe. Waona? Yesu payekha ndi chitsimikizo chokuti Mulungu amasamala za ife.

(Music: underscoring music swells; then begins reprise of Theme music; softly underscoring comments of Program Host during Our Response to God's Word)

OUR RESPONSE TO GOD'S WORD

Program Host

Zikuoneka ngati Filipino salola kuti Tomasi achoke. Poika chikhulupiliro chake mwa Yesu, Filipino wazindikira kuti Mulungu anali akugwira ntchito mkati mwa mnzake watsopanoyu. Ndipo sanalakwitse ai: Mulungu amasamala za Tomasi, m'menendo amasamalira za inu ndi ine.

Chifukwa chiyani, mukhoza kumafunsa; chifukwa Mulungu anatipanga ine ndi ine. Chifukwa anatilenga, ndife apadera kwa Mulungu. Amatikonda ndi chikondi chosatha. Mulungu anamutchula Abrahamu "*mnzanga*" (Yesaya 41:8). Mulungu amamulankhulana Mose "*m'mene munthu amalankhulira ndi mnzake*" (Eksodo 33:11). Ndipo Mulungu ndi mnzathu. Tikhoza kumulankhula ngati mnzathu.

Ndipemphera pemphero lalifupi, lapamtima kwa Mulungu. Inu mvetsarani pemphero langali, ndipo ndikamaliza kupempherako ndikutsogolerani inuyo kuti nanu mupumphere pemphero lomwelo

Wokondedwa Mulungu, zikomo chifukwa munandipanga, chifukwa chimenecho, ndine wapadera kwa Inu. Zikomo chifukwa cha chikondi chanu pa ine. Zikomo chifukwa ndine mnzanu. Ndimakukondani. Amen.

Now repeat the prayer aloud after me. We will pray it a portion at a time. Make the prayer your very own to God. Mean it with all your heart as you pray.

Pano bwerezani pempheroli mokweza kutsatira ine. Tizipemphera modukizadukiza. Inu pempherani motsimikiza, molitanthauza pempheroli ndi mtima wanu onse.

Wokonedwa Mulungu, (dukizani pang'ono kuti munthu akhoza kukutsatizani)

Ndikukuthokozani chifukwa munandipanga, (dukizani pang'ono kuti munthu akhoza kukutsatizani)

ndipo chifukwa, ndine wapadera kwa inu, (dukizani pang'ono kuti munthu akhoza kukutsatizani)

Zikomo chifukwa cha chikondi chanu pa ine. (dukizani pang'ono kuti munthu akhoza kukutsatizani)

Zikomo chifukwa ndine mnzanu. (dukizani pang'ono kuti munthu akhoza kukutsatizani)

Ndimakukondani. Amen. (dukizani pang'ono kuti munthu akhoza kukutsatizani)

Zikomo chifukwa chopemphera pempheroli. Tiphunzira zambiri za Mulungu ndi Chikondi Chake mu pologalamu yotsatira.

(Music: Theme music swells dramatically and fades as broadcast ends)